Republic of Zambia

Ministry of Education

SECONDARY EDUCATION

LITILICA M'CINYANJA

BUKU LOTHANDIZILA MPHUNZITSI

FOMU 1 - TEMU 1

Developed by the Curriculum Development Centre

Lusaka

2025

© Curriculum Development Centre 2025.
All rights reserved. No parts of this publication may be reproduced, stored in a retrieval system or transmitted by electronic, mechanical, photocopying, recording or other means, without the prior permission of the Curriculum Development Centre.

ALEMBI

Rabecca Tembo:	HOD-Languages, Nyamphande Boarding-Lusangazi
Maurine Manda:	Headteacher, Mpezeni park Day Secondary-Chipata
Jelice Sakala:	HOD- Languages, Chasefu Day Secondary Chasefu-Lundazi
Zebron Nyirenda:	Teacher, Petauke Day Secondary- Petauke
Teliza Phiri:	Teacher, Hillside Secondary-Chipata
Nawa Sianga:	Teacher, Misolo Day Secondary-Lusangazi
Juziel Banda:	Retired Headteacher

Zamkati

MAU OYAMBA iv

CIYAMIKO v

CIYAMBI vi

MOGWILITSILA NCHITO BUKULI vii

NJILA ZOPHUNZITSILA vii

MATANTHAUZO A MAU viii

MUTU 1: ZOYAMBILILA M'LITILICA 10

Mutu Waung'ono 1: Matanthauzo A Litilica 10

Mutu Waung'ono 2: Kusanthula Matanthauzo Osiyana-Siyana a Litilica. 12

Mutu Waung'ono 3: Kupanga Matanthauzo Ya Litilica 14

MUTU 2: MITUNDU YA LITILICA 17

Mutu Waung'ono 1: Litilica Ya Zapakamwa 17

Mutu Waung'ono 2: Litilica Ya Zolembedwa 19

Mutu Waung'ono 3: Kusiyana ndi Kufanana kwa Litilica ya Zapakamwa ndi Litilica ya Zolembedwa 21

MUTU 3: NCHITO ZA LITILICA 25

Mutu Waung'ono 1: Litilica Ya Zapakamwa 25

Mutu Waung'ono 2: Litilica Ya Zolembedwa 27

MUTU 4: LITILICA YA ZAPAKAMWA 31

Mutu Waun'gono 1: Mbili Ya Nchito Za Litilica Kucokela Kumakhalidwe Ndi Miyambo (Litilica Ya Zolembedwa Ndi Litilica Ya Zapakamwa) 31

Mutu Waun'gono 2: Mitundu Ya Litilica Ya Zapakamwa 33

BIBLIOGRAPHY 36

MAU OYAMBA

Kubwela kwa maphunziro opindulitsa opatsa maluso ochedwa **Competence Based Curriculum** (CBC) kwabweretsanso msintho pakaphunzilidwe katsopano komanso kothandiza. Maphunzilowa atsopano ali ndi zophunzitsila zomwe zimapangitsa aphunzi kukhala ndi maluso amakono. CBC Iwonetsa ciyambi cotukula maphunzilo komanso kufunikila kwake.

Buku lophunzitsila Litilica M'cinyanja fomu 1 yalembedwa mogwilizana ndi mfundo za amaphunzilo omwe akufuna kulumikiza maphunzilo ndi umoyo watsiku ndi tsiku. Maluso onse omwe apelekedwa mbuku yoonetsa ndondomeko yonse yamaphunziro ya 2023 (**Curriculum framework**) ndi ogwilizana ndi bukuli.

Colinga ca bukuli ndikuthandiza aphunzitsi a maphunzilo a litilica fomu 1 kucilikiza maphunzilo atsopano a CBC Pamene mabuku ololedwa akali osowekela. Bukulili likuonetsa kudzipeleka kosasunthika kwa cigawo ca zamaphunzilo kuti nchito ya aphunzitsi ikhale yapafupi, pakupatsa ndondomeko ya uphungu, nchito zoyeselela ndi mayeso ogwilizana ndi zolinga za CBC. Komabe, aphunzitsi alimbikitsidwa kuonjezele zida zophunzitsila kupyolela mkafuku-fuku kao kuti athane ndi zosowekela zilizonse pomwe agwilitsa nchito CBC.

Ndikhulupilila kuti aphunzitsi azagwilitsa ncito buku limeneli moyenela.

Joel Kamoko (Mr)

Permanent Secretary-Education Servises

Ministry of Education

CIYAMIKO

Buku la litilica mcinyanja yalemdedwa kupyolela mkugawana nzelu ndi kugwilila nchito pamodzi ndi ena. Anthu ambili, zigawo ndi mabungwe anafunsidwa ndi kupatsidwa mpata woti apatse maganizo ao pa uthenga womwe unafunika kukhala mbukuli. Mwaico ndifuna kupeleka mathokozo anga kwa anthu, zigawo ndi mabungwe omwe anapeleka thandizo ya ndalama ndi ukaswili wao kuti buku limeneli lophunzitsila lilembedwe moyenelela. Awa ndi aphunzitsi, aphunzitsi amasukulu apamwamba kwambuli, mabungwe oimilila ziphunzitso (subject associations), Mabungwe akunja kwa boma ndi mabungwe ogwilizana nao.

Pomaliza, ndithokozanso anyanchito a cigawo ca **Curriculum Development Centre** pakutsimikizila kuti nchito yolemba bukuli yamalizidwa moyenelela.

Charles K. Ndakala, (Dr.)

Director Curriculum Development

Ministry of Education

CIYAMBI

Buku lophunzitsila aphunzi fomu 1 yalembedwa mozama kuti ithandizile aphunzitsi kuphunzitsa maphunzio a litilitca mogwilizana ndi maphunziro osinthidwa. Bukuli lalembedwa molingana ndi ndondomeko yovomelezeka ya Cinyanja ya caka ca 2024. Ikufuna kuwongolela kusiyana komwe kunapangidwa cifukwa ca kusowa kwa mabuku ovomelezeka komanso kupatsa aphunzitsi zida zophunzitsila zothandiza, zocita, ndi mayeso yopangidwa kulingana ndi kalasi la ophunzila ndi zosowa zao.

Cigao cazamaphunzilo cidziwa zobvuta zomwe zimabwela cifukwa cosintha maphunzilo atsopano. Kusankha ndondomeko yamaphunzilo opatsa aphunzi maluso osiyana-siyana (**Competence Based Curriculum**) ndi ciyambi ca kusintha pakupititsa patsogolo maphunzilo ndi kufunikila kwake. Bukuli lionetsa kudzipeleka ndi cidwi ca cigawo ca zamaphunzilo kupanga nchito ya aphunzitsi kuti ikhale yotheka pakuwapatsa ndondomeko ya uphungu, nchito ndi mayeso omwe alunjikidwa ndi ndondomeko ya zolinga za maphunzilo atsopano. Komabe, aphunzitsi alimbikitsidwa kuti naonso angathe kuonjezela pakucita kafuku-fuku wao komanso Kupanda zida zao zophunzitsila kuti athane ndi zotsowa zina zomwe zingabuke posewenzetsa ndondomeko yatsopanowa.

Zocita ndi mayeso zomwe zapelekedwa zapangidwa kuti zilimbikitse ndi kukulitsa maluso eni-eni anchito zamanja ndi maluso oganiza mwakuya mwa aphunzi pomwe akuwonetsa kufunikila kwa kugonjela msintho kumalo amaphunzilo osiyana-siyana. Aphunzitsi alimbikitsidwa kugwilitsa nchito uphungu uwu mumakalasi awo osiyana-siyana ndi kufufuza njila zina zololedwa, zobvomerezeka pakafunika kutelo. Kusintha kumeneku ndi kofunikila pakuonetsetsa kuti aphunzi onse, ocokela kumalo osiyana-siyana aphindula ndi maphunzilo abwino atsopano.

Ciyembekezo ndi cakuti bukuli lidzakhala cida cofunikila kwambili kwa aphunzitsi pomwe asewenzetsa ndondomeko yamaphunzilo atsopano

yochedwa Competence Based Curriculum, kukulitsa luso lao lopatsa aphunzi cidziwitso cokwanila cokhudza Cinyanja, maluso omwe angathandize aphunzi kukhala ndi cidwi comwe cingapangitse maphunzilo kukhala aphindu.

MOGWILITSILA NCHITO BUKULI

Bukuli lipeleka uthenga womwe uyenela kuphunzitsidwa mu temu loyamba la Litilicha form 1. Bukuli ndiyogawidwa mzigawo ndipo cigawo ciliconse cili ndi maphunzilo ocokela muzigawo zina zosiyana-siyana zomwe ndi Zoyambilila mu Litilica, mitundu ya Litilica, Nchito za Litilica, Litilica ya Zapakamwa ndi Litilica ya Zolembedwa. Uthenga womwe waikidwa mbukuli siunalembedwe mumaphunzilo, koma uyenela kugwilitsidwa nchito kulemba maphunzilo (lessons). Popanga maphunzilo, muyenela kutenga uthenga kucokela kuzigawo zosiyana-siyana kupanga phunzilo limodzi. Mwacitsanzo, Phunzilo lingakhale ndi kumvetsela ndi kulankhula, matanthauzo a mau, kuwelenga ndi kulemba.

NJILA ZOPHUNZITSILA

Njila zosiyana-siyana zakaphunzitsidwe ziyenela kugwiritsidwa nchito kuti zotsowa zosiyana-siyana za aphunzi zikwanilitsidwe.

MATANTHAUZO A MAU

1. Capamutu-Theme
2. Cidule ca Zili mkati- Overview
3. Cigawo- Component
4. Lambulo-Introduction
5. Gwelo la Uthenga- Reference/Bibliography
6. Kuganiza mwakuya- Critical Thinking
7. Kusanthula maganizo Mwakuya- Analytical Thinking
8. Mgwilizano-Collaboration
9. Kukambitsilana- Communication
10. Kudziwa kugwilitsa nchito zinthu za kopyuta- Digital Literacy
11. Kupanga Zatsopano ndi kuonjezela pa zakale- Creativity and Innovation
12. Zokhuza mwini komanso ena- Emotional intelligence
13. Zamalonda- Entrepreneurship
14. Kuthetsa bvuto-Problem Solving
15. Kukambilana-Discussion
16. Mau acikoka –Hook
17. Kumvetsela ndi Kulankhula- Listening and Speaking
18. Luso lapadela - Specific Competence
19. Luso Lose-General Competence
20. Muyeso oyembekezeleka- Expected Standard
21. Mau ofunika kudziwa i- Key terms
22. Mayeso-Assessment Activities
23. Mutu- Topic
24. Mutu waung'ono- Sub-Topic
25. Mwacidule- Summary
26. Nchito- Learning activities
27. Ntchito yokoka maganizo a aphunzi- Hook
28. Ocita Sewelo- Characters

29. Zinthu zophunzilila ndi Zophunzisila- Teaching and Learning Materials
30. Zindikilani- Note
31. Zocita-Exercise

MUTU 1: ZOYAMBILILA M'LITILICA

Phunziloli linena za Litilica. Litilica idziwika mosiyana-siyana kulingana ndi alembi osiyana-siyana. Ngakhale lidziwika kuti Litilica, imafalitsidwa mnjila zosiyana-siyana kupyolela m'nyimbo, masewelo, ndakatulo, miyambi, mikuluwiko ndi zilapi (ndagi). Izi maka-maka zigwela m'mbali ziwili zimene zili mu zolembedwa komanso zolankhulidwa. Izi ndizofunikila pa umoyo wathu wa tsiku ndi tsiku.

Mutu Waung'ono 1: Matanthauzo A Litilica

Lambulo

Mutuwu ufotokoza za matanthauzo yosiyana-siyana ya Litilica.

Luso Lapadela:

- Kumasulila matanthauzo ya Litilica.

Mau Ofunika Kudziwa:

- ✓ Litilica, luso, kafuku-fuku, mtanthauzila mau…

Mfundo Zophunzitsila:

- ✓ Kumasulila tanthauzo la Litilica.
- ✓ Kupeleka matanthauzo yosiyana-siyana a Litilica.
- ✓ Kucita kafuku-fuku kodziwitsa matanthauzo ena a Litilica.

Zida Zophunzitsila Ndi Zophunzilila:

- Mabuku onena za Litilica yosiyana-siyana.
- Machati olembedwapo matanthauzo ya Litilica.

Nchito

A: Mphunzitsi:

- ✓ Ikani aphunzi m'magulu.
- ✓ Uzani aphunzi kuti apeleke matanthauzo ya Litilica.
- ✓ Uzani aphunzi kuti afotokoze matanthauzo ya Litilica.
- ✓ Uzani aphunzi kuti atanthauzile Litilica.
- ✓ Uzani atsogoleli amagulu kuti apeleke mayankho m'kalasi.
- ✓ Mangilizani mayankho ya aphunzi.

Mwacitsanzo;

- ➢ Litilica ndi njila zofalitsilamo makhalidwe ya anthu ndi zomwe atsatila kupyolela mzolembedwa ndi zapakamwa.

B: Aphunzi:

- ✓ Akhale m'magulu.
- ✓ Apeleke matanthauzo ya Litilica.
- ✓ Afotokoze matanthauzo ya Litilica.
- ✓ Atsogoleli a magulu apeleke mayankho m'kalasi.

Mutu Waung'ono 2: Matanthauzo a Litilica Kulingana ndi Alembi Ena

Litilica ili ndi matanthauzo ambili kulingana ndi alembi osiyana-siyana. Ena mwa matanthauzo odziwika ali motele;

- ✓ Kulingana ndi Magiya Manda m'buku lake lochedwa 'Companion to Literature', Litilica ndi kuphunzila za luso logwilitsa nchito maganizo ndi kafuku-fuku ka zinthu.
- ✓ Kulingana ndi Meyer, ananenanso kuti Litilica ndi nchito zolembedwa kupyolela m'zocitika za tsiku ndi tsiku.

- ✓ Kulingana ndi Mtanthauzila mau (Dictionary) wolembedwa ndi Steven Paas, Litilica ndi zolembedwa ndi zowelengedwa.
- ✓ Litilica ndi njila yofalitsilamo maganizo a munthu mu umoyo wake.
- ✓ Litilica ndi njila imodzi yofalitsilamo za makhalidwe ndi miyambo. Tikati makhalidwe tinena zomwe mtundu umodzi wa anthu ucita ndi zomwe utsatila.

Muyeso Oyembekezeleka :

- Matanthauzo yosiyana-siyana ya Litilica yapelekedwa mokhutilitsa.

- ✓ Matanthauzo yosiyana-siyana ya Litilica yafotokozedwa mokhutilitsa.
- ✓ Litilica yatanthauzilidwa moyenelela.

Mwacidule:

- ✓ M'mutuwu, tanthauzo la litilica lamasulidwa.
- ✓ Matanthauzo yosiyana-siyana ya Litilica apelekedwa.
- ✓ Kafuku-fuku wofufuza matanthauzo ena a Litilica wacitidwa.

Mutu Waung'ono 2: Kusanthula Matanthauzo Osiyana-Siyana a Litilica.

Lambulo:

Litilica ili ndi matanthauzo yambili. Pofuna kudziwa bwino-bwino matanthauza ena a Litilica, pafunika kusanthula mofikapo. Phunziloli lidzasanthula motelo.

Luso Lapadela:

- Aphunzi asanthule matanthauzo ya Litilica yosiyana-siyana.

Mau Ofunikila kudziwa

- Kusanthula, matanthauzo, mofikapo.

Mfundo Zophunzitsila:

- Kusanthula matanthauzo ya Litilica.
- Kulinganiza ndi Kusiyanitsa matanthauzo yosiyana-siyana ya Litilica.
- Kuganizila mozama matanthauzo yosiyana-siyana kwacitidwa.

Zida Zophunzitsila ndi Zophunzilila:

- Mabuku onena za Litilica osiyana-siyana.
- Machati olembedwapo matanthauzo a Litilica.

Nchito

A: Mphunzitsi:

- ✓ Uzani aphunzi kucita kafuku-fuku wa matanthauzo ya Litilica.
- ✓ Funsani aphunzi kupeleka maganizo apadela pa matanthauzo a Litilica.
- ✓ Funsani aphunzi kupeleka maganizo yao pa tanthauzo la Litilica.
- ✓ Lumikizani maganizo ya aphunzi.

  Mwacitsanzo;

  - ➢ Litilica ndi nchito zolembedwa kapena zapakamwa zimene zigwilitsidwa nchito pa umoyo wa anthu.

B: Aphunzi:

- ✓ Acite kafuku-fuku ka matanthauzo ya Litilica.
- ✓ Apeleke matanthauzo ya Litilica yosiyana-siyana kulingana ndi maganizo yao.
- ✓ Apeleke matanthauzo ya Litilica ena kulingana ndi kamvetsedwe kake.

Muyeso Woyembekezeleka:

- ✓ Matanthauza ya Litilica yasanthulidwa mofikapo.
- ✓ Matanthauzo ya Litilica yalinganizidwa ndi kusiyanitsidwa mofikapo.

- ✓ Matanthauzo yosiyana-siyana ya Litilica yasanthulidwa mwandondomeko.

Mwacicule:

- ✓ M'mutuwu kafuku-fuku wa matanthauzo ya Litilica wacitidwa.
- ✓ Matanthauzo ya Litilica apadela apelekedwa.

Mutu Waung'ono 3: Kupanga Matanthauzo Ya Litilica

Lambulo:

Pali matanthauzo yambili ya Litilica. Alembi ambili anatanthauzila Litilica mosiyana-siyana. Motelo, ndikotheka aphunzi kupanga matanthauzo yao-yao.

Luso Lapadela:

- Kupanga matanthauzo ya Litilica yao-yao.

Mau Ofunikila Kudziwa:

- Kupanga, Matanthauzo, Kufalitsa, Kukhudza.

Mfundo Zophunzitsila:

- Kupanga matanthauzo ya Litilica yosiyana-siyana.
- Kulungamitsa matanthauzo ya Litilica yao-yao.

Zida Zophunzitsila Ndi Zophunzilila:

- Mabuku onena za Litilica yosiyana-siyana, machati olembapo matanthauzo ya Litilica yosiyana-siyana.

Nchito

A: Mphunzitsi:

- ✓ Ikani aphunzi m'magulu.
- ✓ Uzani aphunzi kuti apeleke matanthauzo ya Litilica yao-yao.
- ✓ Uzani atsogoleli a m'magulu kuti apeleke mayankho m'kalasi.
- ✓ Uzani aphunzi kuti alungamitse matanthauzo ya Litilica yao-yao.
- ✓ Mangulizani mayankho ya aphunzi.

Mwacitsanzo;

- ➢ Litilica ndi njila yofalitsilamo maganizo ya anthu, makhalidwe ndi miyambo yao. Izi zingakhale zolembedwa kapena zapakamwa.

B: Aphunzi:

- ✓ Akhale m'magulu.
- ✓ Apeleke matanthauzo ya Litilica yao-yao.
- ✓ Alungamitse matanthauzo ya Litilica yao-yao.
- ✓ Atsogoleli a m'magulu apeleke mayankho m'kalasi.

Matanthauzo A Litilica Yao-Yao.

Dziwani kuti ena mwa matanthauzo a Litilica omwe angapelekedwe ndi awa:

- ✓ Litilica ndi kuphunzila za luso logwilitsa nchito maganizo ndi kafuku-fuku ka zinthu.
- ✓ Litilica ndi nchito zolembedwa kupyolela m'zocitika za tsiku ndi tsiku.
- ✓ Litilica ndi zolembedwa ndi zowelengedwa.
- ✓ Litilica ndi njila yofalitsilamo maganizo ya munthu mu umoyo wake.
- ✓ Litilica ndi njila imodzi yofalitsilamo za makhalidwe ndi miyambo. Tikati makhalidwe tinena zomwe mtundu umodzi wa anthu ucita ndi zomwe atsatila.

Muyeso Oyembekezeleka:

- Matanthauzo ya Litilica yao-yao yapangidwa mokhutilitsa.
- Matanthauzo ya Litilica yao-yao yalungamitsidwa moyenelela.

Mwacidule:

- ✓ M'mutuwu, matanthauzo yao-yao ya Litilica apelekedwa mokhutilitsa.

<u>Mayeso</u>

1. Kodi Litilica ndi ciani?
2. Sankha ziganizo ziwili cabe mwa zotsatilazi, zimene zimasulila Litilica:
    a) Litilica ndi zimene zimafalitsidwa kapena kuphunzitsidwa kumibadwo kudzela m'mau olankhulidwa.
    b) Litilica ndi zonse zooneka ndi maso.
    c) Litilica ndi zija zimene zili zolembedwa m'mabuku, m'manyuzipepala, m'majano ndi zina
    d) Litilica ndi zimene zicitika pakati pa anthu.
3. Peleka tanthauzo lako-lako la Litilica.

MUTU 2: MITUNDU YA LITILICA

Zamkati :

Pali mitundu ya Litilica iwili, Litilica ya Zapakamwa ndi Litilica ya Zolembedwa. Litilica ya Zapakamwa ifalitsidwa kupyolela m'kulankhula monga zilapi, masewelo, ndakatulo ndi zina. Litilica ya Zolembedwa ipezeka m'mabuku, zozile moyoko kapena mbili za anthu ochuka ndi zina. Mkatimu mulinso kulinganiza ndi kusiyanitsa kwa mbali ziwilizi za Litilica.

Mutu Waung'ono 1: Litilica Ya Zapakamwa

Lambulo:

Phunziloli linena za tanthauzo la Litilica ya Zapakamwa. Litilica ya Zapakamwa imafalitsidwa mnjila zosiyana-siyana, kupyolela m'nyimbo, masewelo, ndakatulo, miyambi, mikuluwiko ndi zilapi. (ndagi)

Luso Lapadela:

- ✓ Akambilane za Litilica ya Zapakamwa.

Mau Ofunikila Kudziwa:

- ✓ Litilica ya Zapakamwa, mau opotoza lilime, ndagi/ zilapi.

Mfundo Zophunzitsila:

- ✓ Apeleke matanthauzo ya Litilica ya Zapakamwa. Mwacitsanzo:
  - Kulingana ndi Magiya Manda m'buku lake la **'Companion to Literature'**, Litilica ya Zapakamwa ndi zimene zimafalitsidwa kapena kuphunzitsidwa ku mibadwo kupyolela m'mau olankhulidwa.
  - Kulingana ndi Akombo ndi anzake m'buku lawo la 'Golden Tips English for Secondary Schools', Litilica ya Zapakamwa ndi zocita-cita zimene zigwilitsa nchito mau olankhulidwa.
  - Kuwonjezelapo, Litilica ya Zapakamwa ndi khalidwe lophunzitsa miyambo kupyolela m'nkhani, miyambi, nyimbo ndi zikhulupililo.

- Litilica ya Zapakamwa imafalitsidwa mnjila zosiyana- siyana monga kupyolela m'nyimbo, masewelo, ndakatulo…….

✓ Apeze Litilica ya Zapakamwa.

✓ Apange magulu ya mitundu ya Litilica ya Zapakamwa.

✓ Aonetse zizindikilo za Litilica ya Zapakamwa.

✓ Afotokoze Litilica ya Zapakamwa.

Zida Zophunzitsila Ndi Zophunzilila:

✓ Machati woonetsa zithunzi zosiyana- siyana za anthu aimba, abvina…

✓ Machati woonetsa matanthauzo ena ya Litilica ya Zapakamwa.

Nchito

A: Mphunzitsi:

✓ Ikani aphunzi m'magulu.

✓ Uzani aphunzi kuti apeleke matanthauzo ya Litilica ya Zapakamwa.

✓ Uzani aphunzi kuti apeze mitundu ya Litilica ya Zapakamwa.

✓ Uzani aphunzi kuti aike m'magulu mitundu ya Litilica ya Zapakamwa.

✓ Uzani aphunzi kuti aonetse zizindikilo za Litilica ya Zapakamwa.

✓ Uzani aphunzi kuti afotokoze mitundu ya Litilica ya Zapakamwa.

✓ Uzani atsogoleli a m'magulu kuti apeleke mayankho m'kalasi.

✓ Mangilizani mayankho a aphunzi.

Mwacitsanzo;

➢ Litilica ya Zapakamwa ndi ija imene ifalitsidwa kupyolela mu mau apakamwa.

B: Aphunzi:

- ✓ Akhale m'magulu.
- ✓ Apeleke matanthauzo ya Litilica ya Zapakamwa.
- ✓ Apeze mitundu ya Litilica ya Zapakamwa.
- ✓ Aike m'magulu mitundu ya Litilica ya Zapakamwa.
- ✓ Aonetse zizindikilo za Litilica ya Zapakamwa.
- ✓ Afotokoze mitundu ya Litilica ya Zapakamwa.
- ✓ Atsogoleli a m'magulu apeleke mayankho m'kalasi.

Muyeso Oyembekezeleka:

- ✓ Matanthauzo ya Litilica ya Zapakamwa yapelekedwa mokhutilitsa.
- ✓ Mitundu ya Litilica ya Zapakamwa yapezedwa moyenelela.
- ✓ Mitundu ya Litilica ya Zapakamwa yaikidwa m'magulu moyenelela.
- ✓ Zizindikilo za Litilica ya Zapakamwa zaonetsedwa moyenelela.
- ✓ Mitundu ya Litilica ya Zapakamwa yafotokozedwa moyenelela.

Mwacidule:

- ✓ M'mutuwu, tanthauzo la Litilica ya Zapakamwa ndi khalidwe lophunzitsa miyambo kupyolela m'nkhani, miyambi, nyimbo ndi zikhulupililo zamasulidwa.
- ✓ Matanthauzo ena ya Litilica ya Zapakamwa yapelekedwa.
- ✓ Zitsanzo za Litilica ya Zapakamwa zapelekedwa monga nyimbo, ndakatulo……..
- ✓ Zigawo za Litilica ya Zapakamwa zapelekedwa.

Mutu Waung'ono 2: Litilica Ya Zolembedwa

Lambulo:

- Mutuwu ufotokoza za matanthauzo ya Litilica ya Zolembedwa, zigawo zake ndi ziyenelezo zake.

Luso Lapadela:

- Akambilane za Litilica ya Zolembedwa.

Mau Ofunikila Kudziwa:

- Litilica ya Zolembedwa, Zozile moyoko, Tanthauzila mau.

Mfundo Zophunzitsila:

- ✓ Apeleke matanthauzo ya Litilica ya Zolembedwa.
- ✓ Apeze Litilica ya Zolembedwa.
- ✓ Apange magulu ya mitundu ya Litilica ya Zolembedwa.
- ✓ Aonetse zizindikilo za Litilica ya Zolembedwa.

Zida Zophunzitsila Ndi Zophunzilila:

-Mabuku, machati…

Nchito

A: Mphunzitsi:

- ✓ Ikani aphunzi m'magulu.
- ✓ Uzani aphunzi kuti apeleke matanthauzo ya Litilica ya Zolembedwa.
- ✓ Uzani aphunzi kuti apeze Litilica ya Zolembedwa.
- ✓ Uzani aphunzi kuti apange magulu ya mitundu ya Litilica ya Zolembedwa.
- ✓ Uzani aphunzi kuti aonetse zizindikilo za Litilica ya Zolembedwa.
- ✓ Uzani atsogoleli amagulu kuti apeleke mayankho m'kalasi.
- ✓ Mangilizani mayankho ya aphunzi.

Mwacitsanzo;

- ➢ Litilica ya Zolembedwa ndi ija imene ifalitsidwa kapena kuphunzitsidwa kumibadwo kupyolela mu zolembedwa.

B: Aphunzi:

- ✓ Akhale m'magulu.
- ✓ Apeleke matanthauzo ya Litilica ya Zolembedwa.
- ✓ Apeze Litilica ya Zolembedwa.
- ✓ Apange magulu ya mitundu ya Litilica ya Zolembedwa.
- ✓ Aonetse zizindikilo za Litilica ya Zolembedwa.
- ✓ Atsogoleli a magulu apeleke mayankho m'kalasi.

Muyeso Oyembekezeleka:

- ✓ Matanthauzo ya Litilica ya Zolembedwa yapelekedwa mokhutilitsa.
- ✓ Litilica ya Zolembedwa yapezedwa moyenelela.
- ✓ Magulu ya mitundu ya Litilica ya Zolembedwa yapangidwa moyenelela.
- ✓ Zizindikilo za Litilica ya Zolembedwa zaonetsedwa moyenelela.

Mwacidule:

- M'mutuwu matanthauzo ya Litilica ya Zolembedwa yafotokozedwa.
- Zigawo ndi ziyenelezo za Litilica ya Zolembedwa zafotokozedwa mofikapo.

Mutu Waung'ono 3: Kusiyana ndi Kufanana kwa Litilica ya Zapakamwa ndi Litilica ya Zolembedwa

Lambulo:

Mutuwu ufotokoza za kusiyana ndi kufanana kwa Litilica ya Zapakamwa ndi Litilica ya Zolembedwa. Aphunzi afunika kufotokoza za mutuwu mwakuya.

Luso Lapadela:

- Anena kusiyana ndi kufanana kwa Litilica ya Zapakamwa ndi Litilica ya Zolembedwa.

Mau Ofunikila Kwambili:

- Kufanana, Kusiyana

Mfundo Zophunzitsila:

Kufanana kwa Litilica ya Zapakamwa ndi Litilica ya Zolembedwa:

- ✓ Mbali zonse ziwili ziphunzitsa za miyambo.
- ✓ Mbali zonse ziwili zili ndi mkonzi ndi olandila.
- ✓ Mbali zonse ziwili zimasangalatsa.
- ✓ Mbali zonse zigwilitsa nchito mau…

Kusiyana kwa Litilica ya Zapakamwa ndi Litilica ya Zolembedwa:

Litilica Ya Zapakamwa	**Litilica Ya Zolembedwa**
-Ili ndi malile	**-**Ilibe malile
-Idalila pa zolankhulidwa	**-**Idalila pa zolembedwa
-Ingasinthe	-Siingasinthe
-Siidalila ukatswili	-Idalila ukatswili
-Ifunika amvetseli	-Siifunika amvetseli

Zida Zophunzitsila Ndi Zophunzilila;

- Mabuku, machati…

Nchito

A: Mphunzitsi:

- ✓ Aike aphunzi m'magulu.

- ✓ Auze aphunzi kuti apeleke kufanana ndi kusiyana kwa Litilica ya Zapakamwa ndi Litilica ya Zolembedwa.
- ✓ Auze atsogoleli a m'magulu kuti apeleke mayankho m'kalasi.
- ✓ Amangilize mayankho ya aphunzi.

Mwacitsanzo;

- ➢ Litilica ya Zapakamwa idalila pa zolankhula pamene Litilica ya Zolembedwa idalila pa zolembedwa.

B: Aphunzi:

- ✓ Akhale m'magulu.
- ✓ Apeleke kufanana ndi kusiyana kwa Litilica ya Zapakamwa ndi Litilica ya Zolembedwa.
- ✓ Atsogoleli a m'magulu apeleke mayankho m'kalasi.

Muyeso Oyembekezeleka:

- ✓ Kufanana kwa Litilica ya Zapakamwa ndi Litilica ya Zolembedwa kwapelekedwa moyenelela.
- ✓ Kusiyana kwa Litilica ya Zapakamwa ndi Litilica ya Zolembedwa kwapelekedwa moyenelela.
- ✓ Kufunikila kwa Litilica ya Zapakamwa ndi Litilica ya Zolembedwa kwazindikilidwa mokhutilitsa.

Mwacidule:

- Kufanana ndi kusiyana kwa Litilica ya Zapakamwa ndi Litilica ya Zolembedwa kwafotokozedwa mofikapo.

<u>Mayeso</u>

1. Sankha zitsanzo ziwili zimene zinena za Litilica ya Zapakamwa mwa izi:
    a) Buku, zilapi ndi miyambi.
    b) Mbili ya Shaka yokambidwa.
    c) Mbili yolembedwa ya Idiyamini.
    d) Zilapi, miyambi ndi nthano.
2. Ndi cifukwa ciani tiphunzila Litilica ya Zapakamwa? Chula zifukwa ziwili cabe.
3. Nena kusiyana pakati pa Litilica ya Zapakamwa ndi Litilica ya Zolembedwa.
4. Nena kufanana pakati pa Litilica ya Zapakamwa ndi Litilica ya Zolembedwa.
5. Fotokoza ubwino wa Litilica ya Zapakamwa.
6. Fotokoza ubwino wa Litilica ya Zolembedwa.

MUTU 3: NCHITO ZA LITILICA

Zamkati

Pali mitundu iwili ya Litilica. Litilica ya Zapakamwa ndi Litilica ya Zolembedwa. Maguluwa ali ndi nchito zosiyana-siyana. Pali nchito za Litilica ya Zapakamwa ndi nchito ya Litilica ya Zolembedwa.

Mutu Waung'ono 1: Litilica Ya Zapakamwa

Lambulo

- Mutuwu ufotokoza za nchito za Litilica ya Zapakamwa.

Ukatswili Wapadela

- Anene nchito za Litilica ya Zapakamwa.

Mau Ofunikila Kwambili

- Nchito, Ziphuphu, Zotikhudza, Nyengo.

Mfundo Zophunzitsila

- ✓ Nchito za Litilica ya Zapakamwa zinenedwe, mwacitsanzo:
  - Kusunga miyambo ndi cikhalidwe.
  - Kusangalatsa.
  - Kuphunzila ndi kuphunzitsa.
  - Njila yopezelamo cuma.
  - Kukhala pamodzi ndi kudziwika.
  - Kusula ukatswili pa zocita ndi kulankhula.
- ✓ Kufotokoza nchito za Litilica ya Zapakamwa.
- ✓ Kulungamitsa nchito za Litilica ya Zapakamwa.

- ✓ Kufotokoza nchito za Litilica ya Zapakamwa m'kugwebana ndi zotikhuza mu umoyo wathu monga ziphuphu, kusintha kwa nyengo, zamalonda ndi zina.

Zida Zophunzitsila Ndi Zophunzilila:

- Kanema, machati, mabuku...

Nchito

A: Mphunzitsi:

- ✓ Uzani aphunzi kuti achule nchito za Litilica ya Zapakamwa.
- ✓ Uzani aphunzi kuti afotokoze nchito za Litilica ya Zapakamwa.
- ✓ Uzani aphunzi kuti alungamitse nchito za Litilica ya Zapakamwa.
- ✓ Uzani aphunzi kuti anene momwe tingagwilitsile nchito Litilica ya Zapakamwa m'kugwebana ndi zotikhudza mu umoyo wathu monga ziphuphu, kusintha kwa nyengo, zamalonda ndi zina…
- ✓ Mangilizani mayankho ya aphunzi.

Mwacitsanzo;

- ➢ Tigwilitsa nchito Litilica ya Zapakamwa pogwebana ndi zotikhudza monga zamalonda, mwacitsanzo, pakutsatsa malonda pa mawailesi, pa mkwezamau…

B: Aphunzi:

- ✓ Achule nchito za Litilica ya Zapakamwa.
- ✓ Afotokoze nchito za Litilica ya Zapakamwa.
- ✓ Alungamitse nchito za Litilica ya Zapakamwa.
- ✓ Anene momwe tingagwilitsile nchito Litilica ya Zapakamwa m'kugwebana ndi zotikhuza mu umoyo wathu monga ziphuphu, kusintha kwa nyengo, zamalonda ndi zina…

Muyeso Woyembekezeleka

- ✓ Nchito za Litilica ya Zapakamwa zachulidwa moyenelela.
- ✓ Nchito za Litilica ya Zapakamwa zafotokozedwa mofikapo.
- ✓ Nchito za Litilicha ya Zapakamwa zalungamitsidwa mokhutilitsa.
- ✓ Nchito za Litilica ya Zapakamwa m'kugwebana ndi zotikhudza mu umoyo wathu monga ziphuphu, kusintha kwa nyengo, zamalonda ndi zina zafotokozedwa moyenelela.

Cifupikitso

- Mutuwu wafotokoza nchito za Litilica ya Zapakamwa.

Mutu Waung'ono 2: Litilica Ya Zolembedwa

Lambulo

- Mutuwu ufotokoza za nchito za Litilica ya Zolembedwa.

Ukatswili Wapadela

- Anene nchito za Litilica ya Zolembedwa.

Mau Ofunikila Kwambili

- Nchito, Ziphuphu, Zotikhudza, Nyengo.

Mfundo Zophunzitsila

Nchito za Litilica ya Zolembedwa zinenedwe, mwacitsanzo;

- ✓ Kusunga miyambo ndi cikhalidwe.
- ✓ Kusangalatsa.
- ✓ Kuphunzila ndi kuphunzitsa.
- ✓ Njila yopezelamo cuma.

- ✓ Kukhala pamodzi ndi kudziwika.
- ✓ Kusula ukatswili pazocita ndi kulankhula.

Zida Zophunzitsila Ndi Zophunzilila

- Machati, Mabuku...

Nchito

A: Mphunzitsi:

- ✓ Uzani aphunzi kuti achule nchito za Litilica ya Zolembedwa.
- ✓ Uzani aphunzi kuti afotokoze nchito za Litilica ya Zolembedwa mofikapo.
- ✓ Uzani aphunzi kuti aonetse nchito za Litilica ya Zolembedwa m'kugwebana ndi zotikhuza mu umoyo wathu monga ziphuphu, kusintha kwa nyengo, zamalonda, kugwilitsa nchito mankhwala moipa ndi zina…
- ✓ Uzani aphunzi kuti afotokodze nchito za Litilica ya Zolembedwa pocotsa kudalila pa ena ndi kudzetsa kudzidalila m'maganizo.
- ✓ Mangilizani mayankho ya aphunzi.

Mwacitsanzo

- ➢ Tigwilitsa nchito Litilica ya Zolembedwa pakugwebana ndi zotikhudza monga kusintha kwa nyengo, matenda, zamalonda…

B: Aphunzi:

- ✓ Achule nchito za Litilica ya Zolembedwa.
- ✓ Afotokoze nchito za Litilica ya Zolembedwa.
- ✓ Alungamitse nchito za Litilica ya Zolembedwa.

- ✓ Aonetse nchito za Litilica ya Zolembedwa m'kugwebana ndi zotikhudza mu umoyo wathu monga ziphuphu, kusintha kwa nyengo, zamalonda, kugwilitsa nchito mankhwala moyipa ndi zina…
- ✓ Afotokodze nchito za Litilica ya Zolembedwa pocotsa kudalila pa ena ndi kudzetsa kudzidalila m'maganizo.

Muyeso Woyembekezeleka

- ✓ Nchito za Litilica ya Zolembedwa zachulidwa mofikapo.
- ✓ Nchito za Litilica ya Zolembedwa zafotokozedwa mofikapo.
- ✓ Nchito za Litilica ya Zolembedwa zalungamitsidwa mokhutilitsa.
- ✓ Nchito za Litilica ya Zolembedwa m'kugwebana ndi zotikhudza mu umoyo wathu monga ziphuphu, kusintha kwa nyengo, kugwilitsa nchito mankhwala moyipa, zamalonda ndi zina zaonetsedwa moyenelela.
- ✓ Nchito za Litilica ya Zolembedwa pocotsa kudalila pa ena ndi kudzetsa kudzidalila m'maganizo zafotokozedwa mofikapo.

Cifupikitso

- Mutuwu wafotokoza nchito za Litilica ya Zolembedwa.

Mayeso

1. Fotokoza nchito za Litilica ya Zapakamwa ziwili cabe.
2. Fotokoza nchito za Litilica ya Zolembedwa ziwili cabe.
3. Fotokoza m'mene tingagwilitsile nchito Litilica pakugwebana ndi zotikhudza monga:
    a) Ziphuphu.
    b) Kusintha kwa nyengo.
    c) Zamalonda.

4. Kodi ungagwilitsile nchito Litilica motani podzetsa kudzidalila pa iwe wekha?

MUTU 4: LITILICA YA ZAPAKAMWA

Zamkati

Phunziloli linena za zikhulupililo zimene gulu la anthu likhala nazo kusiyana ndi magulu ya anthu ena. Izi zingakhale zolembedwa kapena zapakamwa. Zikhulupililozi zitithandiza kupatula gulu la anthu ku magulu ya anthu ena komanso kuti gululo lidziwike.

Mutu Waun'gono 1: Mbili Ya Nchito Za Litilica Kucokela Kumakhalidwe Ndi Miyambo (Litilica Ya Zolembedwa Ndi Litilica Ya Zapakamwa).

Lambulo

- M'mutuwu mbili ya nchito za Litilica kucokela kumakhalidwe ndi miyambo izafotokozedwa mofikapo.

Ukatswili Wapadela

- Ukambilana za Litilica kulingana ndi makhalidwe ndi miyambo ya anthu.

Mau Ofunikila Kwambili

- Zikhulupililo, ziphunzitso, mbili ya mkhalidwe, miyambo.

Mfundo Zophunzitsila

- ✓ Kuonetsa ubale pakati pa nchito za Litilica (nyimbo, miyambi, ndakatulo, nthano…) ndi mkhalidwe wathu.
- ✓ Kufufudza njila za miyambo zimene zionetsa nchito za Litilica.
- ✓ Kutanthauzila m'mene zopanga-panga zithandizila nchito za Litilica.
- ✓ Kuonetsa ubale pakati pa nchito za Litilica (nyimbo, miyambi, nthano…) ndi mkhalidwe wa anthu kupyolela mu ulamulilo, cipembedzo ndi zauzimu, njila zocitilamo zinthu zamakono…

Zida Zophunzitsila Ndi Zophunzilila

- Mabuku, mapepala a macati, zithunzi-thunzi za mbili zosiyana-siyana.

Nchito

A: Mphunzitsi:

- ✓ Ikani aphunzi m'magulu.
- ✓ Uzani aphunzi kuti aonetse ubale pakati pa nchito za Litilica (nyimbo, miyambi, ndakatulo, nthano…) ndi mkhalidwe wathu.
- ✓ Uzani aphunzi kuti afufudze njila za miyambo zimene zionetsa nchito za Litilica.
- ✓ Uzani aphunzi kuti atanthauzile m'mene zopanga-panga zithandizila nchito za Litilica.
- ✓ Uzani aphunzi kuti aonetse ubale pakati pa nchito za Litilica (nyimbo, miyambi, nthano…)ndi mkhalidwe wa anthu kupyolela mu ulamulilo, cipembedzo ndi zauzimu, njila zocitilamo zinthu zamakono…
- ✓ Uzani atsogoleli amagulu kuti apeleke mayankho m'kalasi.
- ✓ Mangilizani mayankho ya aphunzi.

  Mwacitsanzo;

  - ➢ Ubale umene ulipo pakati pa nchito za Litilica ya Zapakamwa ndi umoyo wathu ndiwakuti nthawi zina ngati mufuna kuphunzitsa, kudzudzula pena kudziwitsa pazocitika za tsiku ndi tsiku timagwilitsa nchito, nchito za Litilica monga nyimbo, miyambi…

B: Aphunzi:

- ✓ Akhale m'magulu.
- ✓ Aonetse ubale pakati pa nchito za Litilica (nyimbo, miyambi, ndakatulo, nthano…) ndi mkhalidwe wathu.
- ✓ Afufudze njila za miyambo zimene zionetsa nchito za Litilica.
- ✓ Atanthauzile m'mene zopanga-panga zithandizila nchito za Litilica.

- ✓ Aonetse ubale pakati pa nchito za Litilica (nyimbo, miyambo, nthano…)ndi mkhalidwe wa anthu kupyolela mu ulamulilo, cipembedzo ndi zauzimu, njila zocitilamo zinthu zamakono…
- ✓ Atsogoleli amagulu apeleke mayankho m'kalasi.

Muyeso Woyembekezeleka

- ✓ Ubale pakati pa nchito za Litilica (nyimbo, miyambi, ndakatulo, nthano…) ndi mkhalidwe wathu waonetsedwa mofikapo.
- ✓ Njila za miyambo zimene zionetsa nchito za Litilica zafufuzidwa mofikapo.
- ✓ Kutanthauzila m'mene zopanga-panga zithandizila nchito za Litilica kwacitidwa moyenelela.
- ✓ Ubale pakati pa nchito za Litilica (nyimbo, miyambo, nthano…)ndi mkhalidwe wa anthu kupyolela mu ulamulilo, cipembedzo ndi zauzimu, njila zocitilamo zinthu zamakono waonetsedwa mofikapo…

Mwacidule

- M'mutuwu, mbili ya nchito za Litilica kucokela kumakhalidwe ndi miyambo yafotokozeledwa mofikapo.

Mutu Waun'gono 2: Mitundu Ya Litilica Ya Zapakamwa

Lambulo

- Mutuwu uchula, ufotokoza ndi kupeleka zitsanzo za mitundu ya Litilica ya Zapakamwa.

Ukatswili Wapadela

- Kukambilana za mitundu ya Litilica ya Zapakamwa.

Mau Ofunikila

- Zilapi, zikhulupililo, ndakatulo, miyambi, nyimbo, nthano…

Mfundo Zophunzitsila

- ✓ Kupeza mitundu ya Litilica ya Zapakamwa (zilapi, zikhulupililo, nthano, ndakatulo, nyimbo, miyambi…).
- ✓ Kutanthauzila mitundu ya Litilica ya Zapakamwa.
- ✓ Kupeleka zitsanzo za mitundu ya Litilica ya Zapakamwa.

Zida Zophunzitsila Ndi Zophunzilila

-Mabuku oyenelela, machati oyenelela…

Nchito

A: Mphunzitsi:

- ✓ Aike aphunzi m'magulu.
- ✓ Auze aphunzi kuti apeze mitundu ya Litilica ya Zapakamwa (zilapi, zikhulupililo, nthano, ndakatulo, nyimbo, miyambi…).
- ✓ Auze aphunzi kuti atanthauzile mitundu ya Litilica ya Zapakamwa.
- ✓ Auze aphunzi kuti apeleke zitsanzo za mitundu ya Litilica ya Zapakamwa.
- ✓ Auze atsogoleli amagulu kuti apeleke mayankho ya magulu.
- ✓ Amangilidze mayankho ya aphunzi.

Mwacitsanzo;

- ➢ Ina mwa mitundu ya Litilica ya Zapakamwa ndi zilapi, zikhulupililo, nthano, ndakatulo, nyimbo, miyambi…

B: Aphunzi:

- ✓ Akhale m'magulu.
- ✓ Apeze mitundu ya Litilica ya Zapakamwa (zilapi, zikhulupililo, nthano, ndakatulo, nyimbo, miyambi…).

- ✓ Atanthauzile mitundu ya Litilica ya Zapakamwa.
- ✓ Apeleke zitsanzo za mitundu ya Litilica ya Zapakamwa.
- ✓ Atsogoleli amagulu apeleke mayankho m'kalasi.

Muyeso Oyembekezeleka

- ✓ Mitundu ya Litilica ya Zapakamwa yapelekedwa moyenelela.
- ✓ Mitundu ya Litilica ya Zapakamwa yatanthauzilidwa mokhutilitsa.
- ✓ Zitsanzo za Litilica ya Zapakamwa zapelekedwa moyenelela.

Mwacidule

- Mutuwu wachula, wafotokoza ndiponso wapeleka zitsanzo za mitundu ya Litilica ya Zapakamwa.

<u>Mafunso</u>

1. Kodi zikhulupililo zili mgulu liti la Litilica?
2. Chula zikhulupililo ziwili zimene udziwa.
3. Chula mitundu iwili ya Litilica ya Zapakamwa imene iphunzitsa za khalidwe.
4. Kodi zopanga-panga monga izi zithandizila bwanji pa nchito ya Litilica ya Zapakamwa?
    a) Ng'oma
    b) Mtolilo
    c) Wezulu
    d) Gitala

BIBLIOGRAPHY

Akombo, S. (2015). *Golden Tips: English for Secondary Schools*. Nairobi: Moran EA Publishers.

Kakonkanya, H. (2015). *Senior Secondary Literature in English*. Lusaka: MK Publishers.

Manda, M. (2018). *Companion to Literature*. Lusaka: Magiya Publishing.

Ministry of Education. (2023). *2023 Zambia Education Curriculum Framework. Lusaka:* Curriculum Development Centre

Ministry of Education. (1977). *Zambian Languages Orthography*. Lusaka: National Educational Company of Zambia (NECZAM)

Ministry of Education. (1996). *Educating Our Future: National Policy on Education*. Lusaka: ZEPH. Available at http://www.moge.gov.zm/?wpfb_dl=55

Paas S. (2013). Dictionary.-Mtanthauzila mau. Blantyre: Christian Literature Action in Malawi (CLAIM)

Roberts, E.V (1988). Literature, an Introduction to Reading and Writing. New Jersey: Prentice Hall.